

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa  
kuchokera m'Baibulo kupita kwa  
amene akulalikira Uthenga Wabwino

## KUITANIDWA KUCHOKA MUMDIMA

*Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, anseme achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za Iye amene anakuitanani mutuluke mumdima, mulowe kuunika kwake kodabwitsa. —1 Petro 2:9*

Uthenga umene wakhala ukutsika kuchokera ku mpando wachifumu wa Mulungu mzaka zonsezi ukadali womwewo ndipo ukukhudzanabe ndi zochitika za mu mbadwo uno. Uku ndi kuitana kuchokera kumwamba kwa Mulungu kuti tichoke mu mdima wa dziko lino lapansi limene lili lauchimo ndipo tilowe mu kuunika kwa choonadi ndi chilungamo. Miyoyo ya anthu yamizidwa mu zikhumbokhumbo zonyansa za thupi monga chigololo, chiwerewere, kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha, utchisi, kupembedza mafano, kudana, kulimbana, chiwawa, kupha, kuledzera, maphwando oipa, ndi zina zambiri. Mdima wauzimu ukuyendayenda padziko pamene anthu akukana Mulungu ndipo akutsata zilakolako za mitima yao. Koma chinthu ichi chidziwike ndi kukhazikika mu mtima wa aliyense kuti “iwo akuchitachita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu.” (Agalatiya 5:19-21).

Anthu akuyesetsa kufuna kuzimitsa liu lamkati la kayeziyezi lochokera kwa Mzimu wa Mulungu lowatsutsa pa zoipa zimene amachita. Iwo amafuna kuti athawe kudzudzulidwa ndi kuweruzidwa kuti alakwa, pamene akuthamangira kuchita zinthu izo zomwe zili zoipa ndi zolakwika ndipo zimabwera pakutsata zofuna za thupi zakanthawi kochepe. Ngakhaleenso ambiri akukana nkomwe zakuti Mulungu aliko komanso kuti nzotheka kwa munthu kukhala moyo wangwiro. Ndipo zipembedzo zokhazikitsidwa ndi anthu zikuyesetsa kukonzanso ndi kutembenuza uthenga wabwino, kuti uchimo ukhoza kupeza malo ndipo choipa chisavute kumanga maziko m'mitima ya anthu. Zoonadi, anthu amakonda mdima kusiyana ndi kuunika chifukwa zochitika zao zili zonyansa (Yohane 3:19).

Zizolowezi zomwe zasantuka chikhalidwe komanso zoipa zosiyanasiyana zakuthupi zilipo pakati pathu, ndipo khalidwe la umunthu likukakatuka pamene mdima ukulowerera. Ngakhale kuti pamapezeka ena amene amaima ndi kusutsana nazo zoipa za nyengo zino, iwo enieniwo amatekeseka ndi kutengedwa ndi zilakolako za kunyada, kudzikweza kapena chuma. Mdima wauzimu m'magawo aliwonse umawalekanitsa anthu ndi Mulungu, ndipo mphotho yake ya uchimo ndi imfa.

Mdima ndiko kusowa kwa kuunika. Koma ku uzimu, ndi mphamvu ya zonse zimene zili zotsutsana ndi Mulungu zimene zimalowerera mwa munthu wamkati; ndipo zimamusokoneza iye kuthupi, kaganizidwe, zakuimvaimva za mthupi, ndiponso kuuzimu. Ntchito za thupi ndi mdima wa uchimo, zimalalitsidwa ndi anthu andale ndi kukometseredwa kudzera mu njira zosiyanasiyana zofalitsira nkhani komanso kudzera mu masewero ndi zosangalatsa za dzikoli, ndipo zikuononga miyoyo ya anthu komanso mabanja. Chikhalidwe cha moyo wauchimo ndi nzeru za dziko lapansi sizikubweretsa chimwemwe, mtendere kapena kukwaniritsidwa mwa anthuwo, koma m'malo mwake izi zikubweretsa moyo wokhala kakasi, kusowa chiyembekezo ndipo pamapeto ake imfa, pamene mtima wa munthu ukulirira chinachake chakuti chikhutitse njala imene ali nayo mkati mwake mwa munthuyo.

Tiyamika Mulungu kuti tikhoza kuombedwa ku uchimo ndi mdima kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu. “Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzake, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse.”

*(Yapitirira pa tsamba 2)*



“Mdima ndiko kusowa kwa kuunika. Koma ku uzimu, ndi mphamvu ya zonse zimene zili zotsutsana ndi Mulungu.”

Mau a Mkonzi

Kalozera wa Baibulo

Osakhala a dziko lapansi

Kuitanidwa ku Chiyero

Kodi Mukudziwa?

3

4

5-6

7

8

Mau a Nyengo Yake

# ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

## Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

## Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

## Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

## Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;  
Aef. 2:1, 5-6

## Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

## Chizalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

## Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;  
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

## Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

## Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;  
Akol. 1:18

## Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

## Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;  
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

## Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

## Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;  
1 Akor. 7:10-11

## Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

## Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;  
Mat. 25:31-46

## Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

## Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

## Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

(1 Yohane 1:7). Kuitana uku ndiko kuchoka mu mdima ndi kulowa mu kuunika kwake kodabwitsa. Kuunikaku ndi kumene kumathamangitsa mdima, ndipo kuunika kwa Yesu Khristu kudzathamangitsa mphamvu ya uchimo kuchokera mumtima. Anthu onse anayenda mumdima ndipo amatsogozedwa ndi mphamvu ya thupi, koma iwo amene amvere kuitana kwa Mulungu, tsopano apeza kuwala ndi mtendere. “Pamenepo Yesu analankhulanso nao, nanena, Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata Ine sadzayenda mumdima, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo.” (Yohane 8:12).



“Ndi bodza la Satana  
kufuna kuwapangitsa  
anthu kuti akhoza  
kusankha, ena mdima  
ndipo ena kuunika.”

Yesu anabwera kuti “yense wokhulupirira Ine asakhale mumdima.” (Yohane 12:46). Ndi bodza la Satana kufuna kuwapangitsa anthu kuti akhoza kusankha, ena mdima ndipo ena kuunika. Ana a Mulungu akuitanidwa kuchoka mu mdima ndipo akuyenera kuyenda monga ana a kuunika, natsimikizira izo zimene zili zovomerezeka kwa Ambuye. Pambali pa kusayanjana ndi zipatso zosapindulitsa za mdima, iwo akuyeneranso kutsutsana nazo (Aefeso 5:8-11).

Pamene munthu wavomereza Khristu ndi mtima wake wonse

nalapa machimo, kuunika kwa Khristu kudzasintha moyo wake. Mau a pa 2 Akorinto 5:17 akhalabe oona amene akuti: “Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano.” Palibenso kunama, kunena bodza, kuchita zadama, ndi chigololo, maudani, kapenanso zina zotere. Kuunika kwa Khristu kudzabweretsa chisomo ndi chipatso cha Mzimu choonetsedwa mu chikondi, mtendere, kukoma mtima ndi zina zotere (Agalatiya 5:22-25); ndipo munthuyo sadzayendanso motsogozedwa ndi thupi koma mwa Mzimu. Pokhala kuti tili ngati ogonera ulendo ndi alendo padziko pano, ana a Mulungu akuuzidwa kuti “mudzikanize zilakolako za thupi zimene zichita nkondo pamoyo” (1 Petro 2:11) ndipo adzipatule ku zadziko lapansi nakhala gawo la mtundu wa oyera mtima.

Kuunika kwa Mulungu kumabweretsa machiritso, kubwezeretsedwanso, mtendere, koma pakuyenera kukhala kusiyana ndi kulekana koonekeratu kuchoka ku mdima. “Ndipo uwu ndi uthenga tidaumva kwa Iye...kuti Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa Iye monse mulibe mdima. Tikati kuti tiyanjana ndi Iye, ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo sitichita choonadi;” (1 Yohane 1:5-6). Sitingakondweretse Mulungu komanso ndikukhala oganiza zakuthupi, nkumayenda monga mwa zofuna za thupi (Aroma 8:5-8).

Ngati mukukhala mu mdima, tsekulani mtima wanu ku kuunika kwa Mulungu ndipo sangalalani ndi madalitso enieni a moyo. ■

*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa [www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org) ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA  
[editor@thegospeltruth.org](mailto:editor@thegospeltruth.org)

# Mau a Mkonzi



*Inu a nyumba ya Yakobo, tiyeni, tiyende m'kuwala kwa Yehova. —Yesaya 2:5*

Pamene dziko lapansi likunka likumirabe mu thope la uchimo, kusiyana pakati pa anthu a dzikoli ndi anthu a Mulungu kukunka kukulirakulira. Kuwala kwa choonadi kuchokera kwa anthu a Mulungu kudzawalabe kwambiri pamene uchimo ukuchuluka. Monga mneneri Yesaya anawapemphera anthu a Mulungu kalero, inenso lero ndikukupemphani kuti: “Tiyeni tiyende m'kuwala kwa Yehova.”

Mutu wa kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi wakuti “Osakhala a dziko lino lapansi.” Sikuti pali zosamveka bwino mu Malemba pankhani yokhudza kuti anthu a Mulungu asiye za dziko lapansi ndipo atsatiye Yesu mu chiyero. Chiyero ndiye mutu wofunikira kwambiri mu chipangano chakale ndi chatsopano, koma ngakhale zili choncho, atsogoleri a masiku ano akufufuta mfundo zokhudza chiyero kudzera ku maulaliki ndi ziphunzitso zao ndi zongofuna kuti anthu amve bwino ndio asangalale. Anthu ambiri, amene amanena kuti ndi a mu mpingo wa Mulungu, akukhala m'moyo wofanana ndi wa dziko lapansi. Ngakhale chisali chotchuka, choonadi chimene chilipo ndi chakuti chiyero ndi choposa zimene munthu amafuna, ndi chinthu chakuti aliyense akhoza kuchichita ngati tikufuna kukondweretsa Mulungu pofuna kuti kumwamba kukhale kwathu.

Oyera mtima a Mulungu akuyenera kuima pa chiyero mu gawo lililonse la moyo pokhala iwo akazembe abwino a Yesu Khristu. Chiyero chenicheni ndi choposa zochitika kunja, ndi chinthu chimene chimachokera ku kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene akukhala mu mtima. Kudzipereka kwenikweni kwa Mulungu kumapangitsa kuti anthu athawe kuchoka ku zinthu ndi mzimu wa dziko ili lapansi. Zoonadi, chiyero ndi chinthu chochitika mu mtima.

Ndimafunitsitsa kuona miyoyo yambiri ikupulumutsidwa ndi kutembenukira kwa Ambuye, komanso mtima wanga ndi wosautsika kwambiri chifukwa cha moyo wosalabadira ndi wosaikirapo mtima umene ali nao anthu ambiri amene amanena kuti ndi Akhristu pa zikhalidwe zoononga za m'dziko lapansi. Mbale wanga, kukhala motumikira Mulungu kutanthauza kuti tifulatire za dziko lapansi ndipo tikhale monga nyimbo ija imanena kuti: “Ine ndasiya zonse za dziko lapansi ndipo ndikutsata Yesu.”

Achinyamata ambiri akupanga zisankho zokhudza zimene adzachite akadzakula, za maphunziro ao, zokhudza banja komanso mavalidwe ndi zina zotero molingana ndi zikhulupiriro komanso zokhumba za dziko lapansi. Chuma ndi kudzitamandira konse kwa dziko lino lapansi sizinunkha kanthu kwa Mulungu amene ali oyera, ndipo sizipereka chimwemwe m'moyo uno ngakhale m'moyo ulinkudza. Tiyeni tidzisunge mu zinthu zauzimu ndi kutsatira izo zimene zili zabwino ndi zopindulitsa ku ubwino wauzimu wa ifeyo komanso ao amene atizungulira.

Anthu enieni a Mulungu amakhalapo ochepa nthawi zonse, ndipo zili chonchonso mu mbadwo uno. Pamene tikhala moyo wachiyero, timachita zinthu, timalankhula, ndipo timavala mosiyana ndi dziko lapansi. Zinthu zimene timachita nao zidzikhala izo zimene zili zokondweretsa kwa Atate Woyera, ndipo zizionetsera chilungamo chake. Ambiri sali okonzeka kuvomereza choonadi chimenechi m'mene chilili osonjezerapo kanthu. Miyoyo yathu isamayezedwe molingana ndi muyezo wa dziko lapansi koma ndi muyezo wodziwika bwino wa chiyero umene uli m'Mau a Mulungu.

Mwana wa Mulungu, sitingathe kukhala ofanana ndi dziko lino lapansi. Tiyeni tifungatire chiyero ndipo tikhazikike miyoyo yathu kwathunthu kwa Mulungu. Tiyeni titaye zinthu zonse zochimwa ndi ziphunzitso zoipa za dziko lino lapansi ndipo tidzipatule ku izo zimene zimabweretsa moyo wosakonda Mulungu. Tiyeni tikhale ndi maganizo a zinthu zakumwamba ndipo tilemekeze Mulungu mu chiyero.

Michael W. Smith

January 2021



*Mukafuna kutipeza*

*pa intaneti, mulembe*

*[www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org)*

*kuti mudzilandira makalata*

*athu kapenanso kuti*

*muone makalata akale.*

**KUDZIPEREKA KWENIKWENI KWA MULUNGU KUDZAPANGITSA  
ANTHU KUTI ATEMBENUKE KU ZINTHU NDI MZIMU WA DZIKO  
LINO LAPANSI. ZOONADI, CHIYERO NDI CHINTHU CHOCHITIKA  
MU MTIMA.**

# Kalozera wa Baibulo

## Mutu: Osakhala a dziko lapansi

**Kuwerenga Malemba:** *Ine ndawapatsa iwo mau anu; ndipo dziko lapansi, linadana nao, chifukwa sakhala a dziko lapansi, monga Ine sindikhala wadziko lapansi. Sindipempha kuti muwachotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo. Siali a dziko lapansi monga Ine sindili wadziko lapansi. —Yohane 17:14-16*

**Mwachidule:** Akhristu akuitanidwa kuchoka mu mdima komanso komanso kuchokera ku dziko lapansi kuti akakhale moyo wachiyero, nayenda mu kuwala kwa Khristu. Iwo akuyenera kukhala osakopeka kapena kulumulidwa ndi zochitika za dziko lapansi ndipo tsiku ndi tsiku iwo akuyenera kulemekeza Mulungu mu zinthu zonse.



### I. Kuitanidwa kuchoka mu mdima

- A. 1 Petro 2:9-11 Kuitanidwa kuchoka mu mdima.
- B. Agalatiya 5:16-25 Anthu ochita ntchito zathupi sadzakalowa Kumwamba.
- C. Yohane 3:19 Anthu amakonda mdima kusiyana ndi kuwala.
- D. 1 Yohane 1:5-7 Simungayanjane ndi Mulungu ndi kuyendanso mumdima. Mwazi wa Yesu utitsuka ife kuchoka ku uchimo wonse.
- E. Yohane 8:12 Otsatira Khristu sadzayenda mu mdima.
- F. Yohane 12:46 Okhulupirira sakhalabe mumdima.
- G. Aefeso 5:8-11 Tsutsani ntchito za Mdima.
- H. 2 Akorinto 5:17 Mwa Khristu, zinthu zonse zakale zapita.
- I. Aroma 8:5-8 Kukhala woganiza zathupi ndi imfa.

### II. Si adziko lapansi

- A. Yohane 17:14-16 Ophunzira a Khristu sali a dziko lapansi.
- B. Yohane 15:18-19 Osankhidwa kuchokera kudziko lapansi. Dziko lapansi lidzakudani.
- C. 1 Yohane 3:1 Dziko lapansi silidziwa kuti ndife ndani.

### III. Musalikonde dziko lapansi

- A. 1 Yohane 2:15 Musalikonde dziko lapansi.
- B. 1 Yohane 2:16 Chilakolako sichichokera kwa Atate.
- C. Akolose 3:1-2 Ikani malingaliro anu pa zinthu zakumwamba.

### IV. Mphamvu ya dziko lapansi

- A. 2 Akorinto 4:4 Mulungu wadziko lino lapansi waphimba maganizo ao.
- B. Akolose 2:8 Kuonongeka kudzera mu nzeru zachabe ndi chinyengo chopanda pake.

### V. Nzeru ya dziko lapansi

- A. 1 Akorinto 3:18-19 Nzeru ya dziko lapansi ndi yopusa kwa Mulungu.
- B. 1 Akorinto 1:18-25 Chopusa cha Mulungu chiposa nzeru za anthu.

### VI. Machenjezo

- A. 2 Timoteo 2:4 Musatanganidwe ndi zochitika za moyo uno.
- B. Aroma 12:1-2 Musafanizidwe ndi dziko lino lapansi.
- C. Yakobo 4:4 Munthu wokonda zadziko lapansi ali mdani wa Mulungu.
- D. Yakobo 1:27 Musadetsedwe ndi dziko lapansi.

### VII. Zotsatira

- A. Mateyu 16:24-26 Kodi munthu apindulanji akapeza dziko lapansi nataya moyo wake?
- B. Agalatiya 6:7-8 Munthu adzakolola kwamuyaya chimene wafesa.

### VIII. Kuitanidwa ku Chiyero

- A. 1 Petro 1:15-16 Khalani woyera pakuti Mulungu ali woyera.
- B. 1 Akorinto 6:18-20 Lemekezani Mulungu m'moyo ndi m'thupi mwanu.
- C. Ahebri 12:14 Opanda chiyero, palibe munthu adzaona Mulungu.

### Kumaliza

*Popeza izi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'chipembedzo. —2 Petro 3:11*

# Osakhala a DZIKO LAPANSI

Otsatira enieni a Khristu akhala komanso mpaka kalekale adzakhala opatukana ndipo ali osiyana ndi dziko lapansi mu khalidwe, cholinga, zochitika, uzimu, mavalidwe ndi moyo wao wa tsiku ndi tsiku. Amene amanena kuti ndi Akhristu koma ali amodzi ndi dziko lapansi amaphwanya mfundo za Iye amene iwowo amanena kuti akumupembedza ndi kumutumikira.



Ngakhale kuti malo ambiri opempherera akhoza kukhala ndi anthu okonda za dziko lapansi amene amanena kuti amakonda Mulungu, mpingo wakumwamba wa Mulungu upangidwa ndi iwo amene anadziperereka kwa Mulungu kwathunthu ndipo moyo wao onse anaupereka kwa Khristu komanso ku

ntchito yake. Popeza ndife alendo pa dziko lapansi, ana a Mulungu amafunabe ntchito kuti azigwira, sukulu kuti aziphunzira, nyumba kuti azikhalamo, komanso ndalama kuti azitha kugula zinthu. Komabe, iwo samafuna chuma cha dziko lapansi koma kuti akondweretse Mulungu tsiku ndi tsiku kudzera mu zimene amakonda, mu nthawi yao, mphamvu zao ndiponso ndi chuma chimene ali nacho panso pano.

## Tili dziko lapansi koma osakhala a m'menemo

Choonadi chozama chokhudza kukhala mwa Mulungu chikupezeka mu pemphero la kwa ophunzira ake limene likuti: "Sindipempha kuti muwachotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo. Siali a dziko lapansi monga Ine sindili wa dziko lapansi." (Yohane 17:15-16). Nkale lomwe, sikuti Mulungu amafuna kuti anthu ake achoke pakati pa anthu onse kenaka ndikukamanga midzi ya anthu oyera mtima okhaokha. M'malo mwake, Yesu amafuna kuti ana ake apite ku dziko lonse lapansi ndipo akalole kuti kuwala kwa choonadi kuwale kwambiri pamene iwo akhala m'moyo wosiyana ndi wachiyero, umene sudetsedwa kapena kukopeka ndi zoipa kapena zochitika zina zimene zawazungulira.

## Tanthauzo la dziko lapansi

Nkofunika kwambiri kuti timvetsetse za maitanidwe komanso zofunikira kuchita kuti tikhale osiyana ndi dziko lapansi. Mau akuti "dziko lapansi" amagwiritsidwa ntchito mu njira zosiyanasiyana mu Malemba. Dziko lapansi likhoza kutanthauza dziko limene timalionali limene Mulungu analilenga; likhoza kutanthauza anthu ake, mwachitsanzo, "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi"; ndiponso likhoza kuimira malamulo, mfundo, zikhulupiriro, zokhumba ndi zonse zimene

anthu osapulumsidwa amalumulidwa nazo komanso zinthu zonse za moyo uno zimene iwowo amakhala akuzifunafuna. Tanthauzo lomalizirali ndi limene Khristu akuligwiritsa ntchito pamene akulengeza kuti ophunzira ake "siali a dziko lapansi." Anthu amene amakhala ndi kuyenda motsatira zikhulupiriro za dziko lino lapansi, amenewo sali ophunzira a Khristu, popeza zoonza zake nzakuti Akhristu salidi a dziko lino lapansi.

## Kudedwa ndi dziko lapansi

Yesu ananena mosajezera kuti dzikoli lidzawada ophunzira ake chifukwa iwowo si a dziko lino lapansi. "koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi, chifukwa cha ichi likudani inu" (Yohane 15:18-19). Anthu a dziko lapansi amakonda zao zokha koma sakonda zolamalira za chiyero kapena kukhala moyo waumulungu. Chifukwa cha ichi, ngati munthu wina akonedwa ndi dziko lapansi, malingana ndi malemba, ameneyo ndi wa dziko lapansi ndipo sakukhala m'moyo wa woyera mtima. Ophunzira a Khristu amayenda mu malamulo a chiyero amene ali osiyana kwambiri ku mzimu komanso zokhumba za anthu amene ali akuthupi ndi osapulumsidwa. "Mwaichi dziko lapansi silizindikira ife, popeza silimzindikira Iye." (1 Yohane 3:1).

## Musalikonde dziko lapansi

Ngakhale kuti pali kuyesetsa kufuna kuti tipeputse chiyero chenicheni posakaniza komanso kuphatikiza mfundo za Khristu ndi mfundo za dziko lapansi, zimene Malemba amafuna ndi zomveka bwino kuti: "Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichili mwa iye." (1 Yohane 2:15). Akhristu akuyenera kuika chikondi chao kwathunthu pa Mulungu sakuyenera kulumulidwa ndi zinthu kapena mzimu wosalungama wa dziko lapansi. Mwana wa Mulungu akuyenera kukhala pamwamba ndi kudzipatula ku zinthu zonse zimene zimakopa anthu kuti adzichita za dziko lapansi ndipo asiye zikhumbokhumboko ndi zizolowezi zoipa, za kudzikuzi, zachilakolako, zongokonda zosangalatsa ndiponso kungofuna ulemu. Chikondi cha dziko lapansi ndi chikondi pa Mulungu sizogwirizana ndipo sizingakhalire limodzi.

*(Yapitirira pa tsamba 6)*

“Pakuti chilichonse cha m’dziko lapansi, chilakolako cha thupi ndi chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo, sizichokera kwa Atate, koma kudziko lapansi” (1 Yohane 2:16). Malemba amanena momveka bwino za zinthu izo zimene zili za dziko lapansi ndipo sizili za Atate. Chilakolako cha maso ndiye zokhumba za zinthu zosangalatsa thupi zimene zili zachimasomaso ndi zodetsedwa ndipo mwa izo pali zina monga mankhwala ozunguza bongo, zoledzeretsa, kukonda kudya, chiwerewere. Dziko lapansi ladzaza ndi chinyanso. Kuvala kugulu zovala zothina kapena zoonetsa thupi ndi zinthu za dziko lapansi ndipo sizigwirizana ndi zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza mavalidwe aulemu ndi osadzikometsera kwambiri. Zodzoladzola ndi zokongoletsa monga zibangiri ndi mikanda zikutsatira mzimu wa dziko lapansi ndipo zimathandizira chikhumbokhumbo cha maso ndi zina zimene zimadyetsa maso. Chikhumbokhumbo chopitirira muyeso chokonda zovala zamtengowapatali ndi zodzionetsera, nyumba komanso galimoto zodula ndi zodzionetsera ndi zinthu zachabe komanso sizochoka kwa Atate. Dama la moyo uno ndi zinthu monga mtima wofuna kutchuka umene umafunafuna kulandira maulemu ndiponso kuchemereredwa ndi anthu. Ili ndi khumbo lofuna kulemekezedwa ndi kupatsidwa ulemere chifukwa cha kulemera ndi chuma cha dziko lapansi.

Zilakolako ndi zikhumbitso zonyansa za dziko lapansi sizigwirizana ndi moyo woyenda ndi Mulungu modzichepetsa ndi mwachikondi. Ngati wina umunthu wake umukokera ku zinthu zimenezi, pali chisomo chakuti akhoza kuzigonjetsa nayamba kuyenda m’ moyo wokondweretsa Khristu. “Chifukwa chake ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Khristu, funani zakumwamba, kumene kuli Khristu wokhala padzanja lamanja la Mulungu. Lingalirani zakumwamba osati za padziko ai.” (Akolose 3:1-2).

### Mphamvu ndi nzeru ya dziko lapansi

Pa 2 Akorinto 4:4 akuphunzitsa kuti “mulungu wanthawi ino ya pansu pano anachititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira.” Pali mphamvu yaikulu ndi machitidwe aakulu mu zinthu komanso mizimu ya dziko lapansi. Ana a Mulungu ambiri atengedwa ndi kuchita nao zinthu za dziko lapansi ndipo potero ataya chikondi chao pa Mulungu. Masewera, maimbdwe, zosangalatsa ndiponso mavalidwe ndi zina mwa milungu yochepa chabe ya dziko lino lapansi imene anthu amaipembedza masiku ano, popeza imalamulira zimene anthu amayenera kuzikonda, nthawi komanso ndalama zao. Mphamvu yaikulu ya dziko lapansili sili mu zinthu zimenezi, koma mu nzeru ndi kaganizidwe. “Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati chuma, mwakukonda nzeru kwake, ndi chinyengo chopanda pake, potsata mwambo wa anthu, potsata zoyamba za dziko lapansi, osati potsata Khristu” (Akolose 2:8).

Ana a Mulungu akuyenera kusamala, kupanda apo adzapotozedwa mu kaganizidwe kao kuchoka pa moyo wachiyero wa tsiku ndi tsiku. Iwo akhoza kubedwa pomvera zonena za anthu akuthupi, amene Mulungu alibe naye ntchito. Aphunzitsi ndi alangizi osapulumsidwa a m’nthawi yathu ino akhoza kuonetsa ngati ali ndi chidziwitso komanso kumvetsetsa kozama ndipo amakhala

ngati ndi anzeru kwambiri mwakuti amapeputsa umulungu polimbilikitsa kaganizidwe kakuti munthu akhoza kuganiza chilichonse kuonjezapo ngakhale pa zinthu zimene zili zotsutsana ndi umulungu.

Paulo mtumwi analemba kwa mpingo wa ku Korinto nawachenjeza pa 1 Akorinto 3:19 kuti: “Pakuti nzeru ya dziko lino lapansi ili yopusa kwa Mulungu. Pakuti kwalembedwa, Iye agwira anzeru m’chenjerero lao.” Uthenga wa kulalikira za mtanda ndi chopusa ku dziko lapansi, koma ndi mphamvu ya Mulungu; ndipo “Chifukwa kuti chopusa cha Mulungu chiposa anthu ndi nzeru zao; ndipo chofooka cha Mulungu chiposa anthu ndi mphamvu yao.” (1 Akorinto 1:18-25). Kodi mukumvera ndani kuti akulangizeni ndi kukutsogolerani? Mu dziko lino pali dongosolo lapaderadera limene limawakankhira anthu kutali ndi chiyero. Samala, iwe mwana wa Mulungu!

### Machenjezo

Pakuyenera kukhala chenjezo lalikulu pamene tikukhala mu dziko lapansi kuti tisakhale a ilolo. “Msilikali sakodwa nazo ntchito wamba,” (2 Timoteo 2:4). Zimenezi zikuphatikizapo zandale ndi zina zochitika mu dziko. Posakhalitsa, mzimu wakuthupi ukhoza kubwera ndi kulowa mu chinthu chabwino ndipo ndi kuononga mzimu komanso khalidwe zimene poyamba zinali zopatulikira Mulungu.

Mpingo wa ku Roma, unapatsidwa chobetchera, chomwenso chili ndi mpingo wathu lero, kuti udzipereke kwathunthu kwa Mulungu pomwe anati, “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansu pano: koma mukhale osandulika, mwakukonzanso kwa mtima wanu,” (Aroma 12:1-2). Mitima yambiri ikufunika kuti ikonzedwensu chifukwa pali Akhristu ochuluka amene akuchita zinthu mofanana ndi dziko lapansi mu cholinga, mzimu, ndi m’makhalidwe; ndipo izizi sizovomerezeka kwa Mulungu. Mau amphamvu ndi oona amene ali pa Yakobo 4:4 akunena kuti: “Potero, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu.” Ngakhale kuti chiphunzitsa cha atsogoleri ampingo ambiri chasungunulidwa, komabe chipembedzo chosadetsedwa ndi ichi chakukhala “wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi” (Yakobo 1:27).

Maso a anthu ambiri amene ali akhungu ku uzimu atsekuke ku zoopsa za dziko lapansi kuti potero akhoza kuona kukongola kwa chiyero. Mnzanga wowerengawe, dzifufuze moyo wako molingana ndi mau a Mulungu. Kodi mwinjiro yako ili yodetsedwa ndi dziko lapansi kapena ukhoza kunena ndi chikumbumtima choona pamaso pa Mulungu kuti, “Si ine wa dziko ili lapansi monga momwe Khristu sanali wa dziko lapansi”? Kodi uli wokonzeka kukhala wosiyana ndi dziko lapansi, ndi banja lako, ndi anzako ndipo kuti uime limodzi ndi Yesu? Kodi zikupindulira chiyani, ngati utapeza dziko lonse lapansi koma ndikutaya moyo wako? (Mateyu 16:24-26).

Posakhalitsa, dziko lapansili lipita, ndipo iwo amene analitsatira adzazunzika ku imfa ndi chilango chamuyaya, pamene moyo wosatha, kudzera mwa Khristu ukudikira mwana wa Mulungu amene “sali wa dziko lapansi”. ■



Kukhala m'moyo wa chiyero mwa Ambuye ndiko kukhala m'moyo wokwaniritsidwa. Pamene tichita zimene Mlengi wathu anatilamulira komanso anatikonzera zimabweretsa chimwemwe chachikulu komanso zimapangitsa kuti tikwaniritse zimene Iye anatilengera kuti tidzachite. Ngakhale pali njira zambiri, komabe imodzi yokha ndi imene imakafika ku moyo wosatha. Indedi, iyi ndi njira yopapatiza ndipo ndi ochepa okha amene amayendamo, komatu ndi njira yabwino. Kuyenda mu mseu wa chiyero kumabweretsa mpumulo ndi mtendere weniweni mumtima, popeza ndi mkupezeka kwa Ambuye momwe munthu amapezamo kukwaniritsidwa kwenikweni. Tikhoza kumupeza Mulungu mu moyo wa chiyero, popeza Iye ndi Mulungu woyera. Anthu ambiri amafunafuna Mulungu posakaniza mzimu wa dziko lapansi ndi mfundo zabwino za moyo. Izi zikuonekera pamene nyimbo zambiri zooneka zauzimu ndi zachipembedzo mu dziko lapansi zimene zimagwiritsa ntchito mau a Mulungu osakaniza ndi maimbidwe a dziko lapansi pongofuna kuti anthu atengeke. Zoonadi, chiyanjano chokhalitsa mwa Mulungu sichipezeka mu kusakanizaku koma mu ungwiro ndi chiyero.

Kuyambira poyambirira, cholinga cha Mulungu chinali chakuti akhale ndi anthu amene ali opatulika ndi oyera, ndipo adzipereke ku kulambira Mulungu. Mfundo yeniyeni ya chiphunzitso cha Khristu inakhazikika pa chiyero. Iye analangiza ophunzira ake za mmene angawalitsire ulemerero wa Mulungu ku dziko lapansi limene lili lotayika.

“Komatu monga Iye wakuitana inu ali woyera mtima, khalani inunso oyera mtima m'makhalidwe anu onse; popeza kwalembedwa, Muzikhala oyera mtima, pakuti Ine ndine woyera mtima” (1 Petro 1:15-16). Tikuitanidwa kuti tikayende ndi kukhala m'moyo wachiyero, umene popanda iwowo, simungakhale mu moyo woyanjanitsidwa ndi Mulungu. Chiyero chenicheni, chimene chimachokera kwa Khristu mwini, chimatithandiza ndi kutipangitsa kuti tiyende m'moyo wokondweretsa Ambuye. Tikuyenera kukhala woyera mu gawo lililonse la moyo wathu. Tikati woyera sizitanthauza kokha kukhala “opatulika” koma kukhala “chimodzimodzi nthawi zonse.” Moyo wa Mkhristu

ukuyenera kukhala umodzimodzi womwewo wa mu mzimu ndi mcholinga, kaya ndi wakunja kapena wamkati.

Pa 1 Akorinto 6:20 akunena kuti: “Pakuti munagulidwa ndi mtengo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu.” Kulemekeza Mulungu ndicho chotchinga chimene chimakuta madera onse a moyo wathu: kuyambira pa zimene zimatifulumiza kuti tipange zisankho, komanso mau amene timalankhula, machitidwe athu pa zinthu, ngakhalenso m'mene timavalira kunjira. Ana a Mulungu akuitanidwa kuti alemekeze Mulungu mu njira iliyonse, tsiku lililonse.

Mdaniyo adzayesetsa kuonetsa chiyero ngati kukhala moyo wamalamulo monga, “Simungachite izi, simungachitense izozo. Simungapite uko, simungamvere izo”. Mdaniyo ndi wabodza. Chiyero chimamasula, osati kuletsa. Chiyero kudzera mwa Khristu chimamuthandiza Mkhristu kuti akhale womasuka ku mphamvu za dziko lapansi zimene zimatsogolera ndi kuongolera anthu. Chipulumutso ndi chiyero chenicheni chimatimasula ife kuchoka ku mantha ndi chizunzo. Monga m'mene imanenera nyimbo ina, chiyero chimabweretsa, “mtendere m'malo mwa udani, nsanje ndi chiwawa.” Chiyero chikhudzana kwambiri ndi zimene tikhoza kuchita mwa Khristu kusiyana ndi zimene sitingachite mu dziko lapansi.

Kukhala m'moyo wachiyero, ndiwo maitanidwe apamwamba kwambiri, ndipo zimaposa m'mene anthu ambiri amakhalira pakati pathu. Zimatengera kulimba mtima ndi chamuna kuti munthu avomere maitanidwe akuti akhale wopatulika, koma phindu lake nlamuyaya. Nkofunika kwambiri kuvomera maitanidwe akuti tikhale oyera, popeza popanda chiyero “palibe mmodzi adzaona Ambuye” (Ahebri 12:14). ■

“Moyo wa Mkhristu ukuyenera kukhala umodzimodzi womwewo wa mu mzimu ndi mcholinga.”

“PAKUTI MULUNGU SANAITANE IFE TITSATE CHIDETSO, KOMA CHIYERETSO.”

1 ATESALONIKA 4:7



KODI MUKUDZIWA?

Kuchokera mu zolemba za munthu wotchedwa Tertullian mzaka za m’ma 210 AD, iye akuti: “Ngati munthu ukukhulupirira kuti ndiwe Mkhristu, uli wosiyana ndi munthu wachikunja. Muloleni iye achite monga amaganizira! Komanso, pajatu iyeyo akuyenera kuphunzira kuchokera ku m’mene mumachitira zinthu. Nanga nchifukwa chiyani mukudalira kuti mutsogozedwe ndi wosaona pamene inuyo muli ndi maso anuanu? Bwanji mukuvekedwa ndi iye amene ali wamaliseche, ngati inuyo mwavala Khristu?”




Mau a Nyengo Yake

## MLALIKI WA CHILUNGAMO

*Ndipo sanalekerere dziko lapansi lakale, koma anasunga Nowa mlaliki wachilungamo, ndi anzake asanu ndi awiri, pakulitengera dziko la osapembedza chigumula. —2 Petro 2:5*

Nowa, pofuna kumvera langizo lochokera kwa Mulungu, anagwira ntchito mokhulupirika pomanga chombo chomwe chinatenga zaka zochulukira. Chombo chimenechi chinali njira yopulumukira ku chigumula chimene chinali kudzaononga anthu ochimwa malingana ndi chiweruzo cha Mulungu. Ngakhale amasekedwa ndi kunyozedwa, Nowa anapitirirabe kukhala m’moyo wangwiro pamaso pa Mulungu ndipo sanafune kugonjera ku moyo wachisawawa umene anthuwo amakhalamo. Analipo yekha amene anakhulupirira kuti Mau a Mulungu anali choonadi. Iye “anamanga chingalawa cha kupulumutsiramo iwo a m’nyumba yake nakhala wolowa nyumba wachilungamo chili monga mwachikhulupiriro” (Ahebri 11:7).



Pa Genesis 6:9 akutiiza kuti “Nowa anali munthu wolungama ndi wangwiro m’mbadwo yake; Nowa anayendabe ndi Mulungu.” Nzachidziwikire kuti Nowa sanangokhala munthu wachikhulupiriro koma anali mlaliki wa chilungamo. Iye analalikira za choonadi ndi chilungamo kudzera muntchito ndi mumau. Kunali kosavuta kwa iye kuti asalabadire zimene zimachitika koma Nowa anaona kuipa kwa mtundu wa anthu ndipo analalikira za chilungamo kwa anthuwo pofuna kuwapatsa mwai wakuti adzichepetse nalape machimo ao chiweruzo cha Mulungu chisanawafikire.

Pali kufunikira kwakuti mu mbadwo wathu uno umene uli wopotoka, tikhale ndi alaliki ambiri achilungamo. Alaliki ambiri amalalikira zinthu zongofuna kuti anthu amve bwino, ngakhale anthuwo ali mu uchimo, Iwo amaphunzitsa zinthu zimene ndi zosavuta kuzimva ndi kuzilandira. Mulungu ndi woyera ndipo atumiki ake akuyenera kukhala alaliki a chiyero komanso odzipatula ku zoipa ndi mzimu wonyansa wa dziko lino lapansi. Mlaliki wa chilungamo akhoza kunyogodoledwa, kunyozedwa ndi kuzunzidwa. Padzakhala anthu amene adzachoka mu mpingo chifukwa chakuti akhumudwa. Komabe, nkwabwino kuti anthu akhumudwe m’moyo uno chifukwa chakuti tikufuna kuwapatsa mpata kuti alape kusiyana ndi kuti adzakhumudwe kwamuyaya pa tsiku la chiweruzo komanso osakhala ndi mwai wakupulumuka.

Monga m’mene zinaliri m’masiku a Nowa, momwemonso zidzakhala chimodzimidzi pa tsiku lomaliza la chiweruzo. Oyera mtima adzapulumuka, pamene oipa adzadulidwa napita ku imfa yamuyaya. Mulungu awapatse Mzimu Woyera atumiki onse kuti akhoza kulimba mtima nalalikira choonadi chonse cha chiyero popanda kupsatira, popeza chimenechi ndi chomwe chimapulumsa moyo. ■

### Kuti Mutipeze

The Gospel Truth  
P. O. Box 2042  
Nixa, MO 65714  
USA

Email:  
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE